## PHUNZIRO LA 33

1. Kodi Mulungu analonjeza chiyani kwa Mose atalankhula kwa iye kuchokera mu chithukuluzi chimene chimkayaka koma osapselera chija?
-Mulungu analonjeza kuti adzamubweretsanso Mose pa phiri la Sinayi.

2. Kodi Mulungu analisunga lonjezo lake lakuti adzamubweretsanso Mose pa phiri la Sinayi?
-Inde.

3. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamuyitana Mose kuti apite pamwamba pa phirilo?
-Chifukwa chakuti Mulungu ankafuna kulankhulana ndi Mose.

4. Kodi Mulungu anamuwuza chiyani Mose pamwamba pa phiri paja?
-Mulungu amkafuna kupereka chipangano kwa a Isirayeli.

5. Kodi chipangano chimene Mulungu anapereka kwa a Isirayeli chinali chotani?
-Mulungu anati kuti ngati a Isirayeli akuŵamvera malamulo a Mulunguyo, Iye adzaŵadalitsa iwowo.

6. A Isilayeli anakakhala kuti saŵatha kuŵamvera malamulo onse a Mulungu, kodi Mulungu anakachita chiyani?
-Mulungu anakaŵapatsa chilango a Isilayeli.

7. Kodi a Isirayeli anamuwuza chiyani Mulungu?
-A Isirayeli anamuwuza Mulungu kuti adzaŵamvera malamulo onse a Mulunguyo.

8. Kodi a Isilayeli ankayikumbukira nthaŵi imene iwo sankamumvera Mulungu kalekale?

-Iyayi.

9. Kodi a Isirayeli ankaganiza zakuti adziŵamvera malamulo onse a Mulungu?
-Inde.

10. Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli ankaganiza zakuti aŵatha kuŵamvera malamulo onse a Mulungu?
-Chifukwa chakuti iwowo anali adzikonda ndipo adzikweza.

11. Kodi a Isirayeli anakatha kuŵamvera malamulo onse a Mulungu?
-Iyayi.

12. Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli sanakatha kuŵamvera malamulo onse a Mulungu?
-Chifukwa chakuti anabadwa ali ana a Adamu ndi Hava.
-Chifukwa chakuti anabadwa ali akapolo a tchimo.
-Chifukwa chakuti anabadwa ali akapolo a Satana.

13. Kodi Mulungu ankadziŵa kuti a Isirayeli satha kuŵamvera malamulo onse a Mulunguyo?
-Inde.

14. Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anakhazikitsa chipangano ndi a Isirayeli Iye akudziŵa kuti iwowo sakwaniritsa chipanganocho?
-Mulungu anakhazikitsa chipanganocho chifukwa chakuti Iye ankafuna kuŵaphunzitsa chilungamo chofunika kwambiri a Isirayeli.

15. Kodi ndi chiyani chemene Mulungu ankafuna kuŵaphunzitsa a Isirayeli?
-Mulungu ankafuna kuŵaphunzitsa a Isirayeli kuti iwowo sangathe kuŵamvera malamulo Ake onse.



-Munthu sangathe kuziwona m'mene nkhope yake ilili asanaziyang'anire pa kalilole, chomchonso ife sitingathe kuziwona kuyipa kwathu kapena kuyipa kwa mitima yathu tisanayang'ane m'malamulo a Mulungu.

-Mulungu anapereka malamulo ake kuti aŵawonetse a Isilayeli mitima yawo yoyipa ija ndi machimo awo omwe.

-Mulungu anapereka malamulo ake kuti atiwonetse ife kuyipa kwa mitima yathu ndi machimo athu omwe.

-Mulungu anapereka malamulo ake kuti aŵawonetse anthu onse kuyipa kwa mitima yawo ndi machimo awo omwe.

-Chifukwa chakuti mitima yathu ndi yoyipa ndi machimo, chomcho palibe china chilichonse chovomerezeka chimene ife tingachite.

-Chifukwa chakuti mitima yathu ndi yoyipa ndi machimo, palibe chimene ife tingachite kuti timuyandikire Mulungu.

-Chifukwa chakuti mitima yathu ndi yoyipa ndi machimo, palibe chimene ife tingachite mwatokha kuti tivomerezedwe kwa Mulungu.

-Sizingatheke kuti tidziyeretse tokha mitima yathu yoyipayi.
-Kodi ndi ndani amene angathe kuyiyeretsa mitima yathu yoyipa ndi machimoyi?
-Mulungu yekha.

-Ngakhale titaŵamvera malamulo onse a Mulungu, ndikusalimvera lamulo limodzi lokha, Mulungu akulankhula kuti ndi chimodzimodzi ndi kusaŵamvera malamulo ake onse.

-Kodi Satana sanamumvere Mulungu kangati, Mulunguyo asanamuthamangitse Satanayo kumwamba ndi kumukonzera iye njanja ya moto wosatha?
-Kamodzi.
-Satana anachimwa kamodzi koma Mulungu anamupatsa chilango cha imfa.

-Kodi angelo amene ankamutsatira Satana, sanamumvere Mulungu kangati, Mulunguyo asanaŵathamangitse angelowo kumwamba ndi kuŵakonzera njanja ya moto wosatha?
-Kamodzi.
-Angelo amene ankamutsatira Satana, anachimwa kamodzi koma Mulungu anaŵapatsa chilango cha imfa.

-Kodi Adamu ndi Hawa sanamumvere Mulungu kangati, Mulunguyo asanaŵachotse iwowo m'munda mwa Edeni muja?
-Kamodzi.

-Adamu ndi Hawa anachimwa kamodzi koma Mulungu anaŵapatsa chilango cha imfa.

-Mulungu ndi woyera mwakuti ngakhale tchimo limodzi, liyenera kulandira chilango cha imfa.

-Malamulo a Mulungu ali ngati kalilole.

-Kodi malamulo a Mulungu ali ngati kalilole mu njira yanji?
-Amatiwonetsa ife machimo athu.
-Amatithandiza ife kuti tidziŵawona machimo athu.



-Mulungu ankafuna kuŵaphunzitsa a Isirayeli kuti iwowo sangathe kuŵamvera malamulo onse a Mulungu chifukwa chakuti iwowo anabadwira mu tchimo.
-Mulungu ankafuna kuŵaphunzitsa a Isirayeli kuti chifukwa chakuti iwowo sanakatha kuŵamvera malamulo onse a Mulungu, Mulungu yekha ndi amene anakatha kuŵapulumutsa iwowo ku imfa yosatha.

16. Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli anakafa anakalikhudza phirilo?
-Chifukwa chakuti Mulungu ankatsika pa phiripo.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi oyera.
-Chifukwa chakuti Mulungu amadana ndi tchimo lina lililonse.
-Chifukwa chakuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lina lililonse ndi imfa.

17. Kodi chifukwa chiyani a Isilayeli ankaliwopa phiri lija?
-Chifukwa chakuti mabingu anagwedeza mlengalenga onse wozungulira phirilo.
-Chifukwa chakuti mphezi inang'anima pa malo ponse pozungulira phirilo.
-Chifukwa chakuti utsi wakuda kwambiri unavundikira pamwamba ponse pa phirilo.
-Chifukwa chakuti phiri lonse linagwedezeka kwambiri.
-Chifukwa chakuti Mulungu anatsika m'moto pamwamba pa phirilo.

18. Kodi mabingu, mphezi, utsi ndi moto zinali zizindikiro za chiyani?
-Mulungu ndi woyera.
-Mulungu amadana ndi tchimo.
-Mulungu amapereka chilango pa machimo onse ndi imfa.

-Musa atatha kulunkhulana ndi Mulungu, iye anatsika mphirimo.

-Mabingu anapitiriza kugwedeza mlengalenga onse wozungulira phirilo.
-Mphezi inapitiriza kung’anima pa malo ponse pozungulira phirilo.
-Utsi wakuda kwambiri unapitiriza kuvundikira pamwamba ponse pa phirilo.
-Phiri lonse linapitiriza kugwedezeka kwambiri.

-A Isilayeli sanaliyandikire phirilo chifukwa chakuti ankawopa kwambiri.

-Kenako Mulungu analankhula ndi a Isilayeli kuchokera mphirimo.

-Izi ndi zimene analankhula Mulungu:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:1-2

1-Mulungu analankhula mawu onsewa, anati:
2-“Ine ndi Ambuye, Mulungu wako amene ndinakutulutsa mu ukapolo, mdziko la Iguputo.”

-Kuchokera pa phiri la Sinayi, Mulungu anamupatsa Mose Malamulo khumi.

-Ili ndiye lamulo loyamba limene Mulungu anapereka.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:3

3-“Musakhale ndi milungu ina, koma Ine ndekha.”

-Mu lamulo loyamba, Mulungu akulamula kuti Iye yekha ndiye Mulungu wathu.



-Kodi chifukwa chiyani Mulungu akuti ife tisamazifune zinthu zimene anthu ena alinazo?
-Chifukwa chakuti Mulungu mwini ndi amene wazipereka zimenezo kwa anthu enawo.

-Ngati tikuzifuna zinthu zimene anthu ena alinazo, ndiye kuti tikuliphwanya lamuloli.

-Mulungu akulankhula kuti anthu onse aphwanya lamuloli.

-Chilango chophwanya lamuloli ndi imfa yosatha mu nyanja ya moto wosatha.

-Aŵa ndiye malamulo khumi amene Mulungu anapereka kwa a Isilayeli.

-Malamulo amene Mulungu anaŵapereka kwa a Isilayeliŵa, ndi malamulo amene Mulungu anaŵapereka kwa anthu onse.

-Palibe munthu amene angathe kuŵamvera bwino bwino malamulo onseŵa.

-Ife tonse taphwanya malamulo a Mulungu.

-Kodi chilango chaphwanya malamulo khumi a Mulungu ndi chotani?
-Imfa mu nyanja ya moto wosatha.

-Kodi chilango chophwanya limodzi mwa malamulo a Mulunguŵa ndi chotani?
-Imfa mu nyanja ya moto wosatha.

-Ili ndiye lamulo lachisano ndi chinayi limene Mulungu anapereka:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:16

16-“Musapereke umboni womunamizira mzanu.”

-Mu lamulo lachisano ndi chinayi, Mulungu akutilamula ife kuti tisamaname.

-Kodi chifukwa chiyani akuti tisamaname?
-Chifukwa chakuti bodza silochokera kwa Mulungu.
-Chifukwa chakuti bodza limachokera ku tchimo ndipo kwa Satana.

-Ngati sitikunena zowona , ndiye kuti taphwanya lamuloli.

-Ngati tikudziŵa zowona ndikulephera kunena zowonazo, ndiye kuti tanama, chomcho ndiye kuti taphwanya lamuloli.

-Mulungu akulankhula kuti anthu onse aphwanya lamuloli.

-Chilango chophwanya lamuloli ndi imfa yosatha mu nyanja ya moto wosatha.

-Ili ndiye lamulo lakhumi limene Mulungu anapereka:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:17

17-“Musakhumbire nyumba ya nzanu. Musakhumbire mkazi wa nzanu, ngakhale wa tchito wake wa mamuna kapena wa mkazi, ngakhalenso bulu wake kapena chinthu china chilichonse cha nzanu.”

-Mu lamulo lakhumi, Mulungu akutilamula ife kuti tisamazifune zinthu zimene anthu ena alinazo



-Kodi chifukwa chiyani Mulungu yekha ndi amene ayenera kukhala Mulungu wathu?
-Chifukwa chakuti kuli Mulungu m’modzi yekha.
-Chifukwa chakuti kulibenso Mulungu wina.

-Pa nthaŵi imene ife timagwadira mizimu, ndiye kuti ife tikuyitsogoza mizimuyo m’malo mwa Mulungu wathu, chomcho timakhala tikuphwanya lamuloli.

-Ngati ife tikukhulupirira zithumwa, ndiye kuti ife tikuzitsogoza zithumwazo m’malo mwa Mulungu wathu, chomcho timakhala tikuphwanya lamuloli.

-Ngati ife tikuyenda mjira zathu m’malo moyenda mu njira ya Mulungu, ndiye kuti tikuzitsogoza tokha m’malo mwa Mulungu, chomcho tikuliphwanya lamuloli.

-Ngati sitikumulola Mulungu kuti akhale Mulungu wathu m’masiku athu onse, ndiye kuti tikuliphwanya lamuloli.

-Mulungu akulankhula kuti anthu onse aphwanya lamuloli.

-Chilango chophwanya lamuloli ndi imfa yosatha mu nyanja ya moto wosatha.

-Ili ndilo lamulo lachiŵiri limene Mulungu anapereka:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:4-5

4-“Musadzipangire nokha chinthu china chilichonse chosema, ngakhale kupanga chinthu chofanana ndi chinthu china chilichonse cha kumwamba, kapena pa dziko la pansi, kapena chinthu chimene chili pansi pa madzi a pansi pa dziko.
5-Musadzigwadire kapena kudzipepherera zimenezi, pakuti Ine Ambuye, Mulungu wanu, sindikulorani kuti

mukhale ndi milungu yina. Ndiponso ndikupereka chilango kwa ana chifukwa cha kuchimwa kwa makolo awo, mpaka m’bado wa chitatu ndi chinayi wa anthu amene akudana ndi Ine.”

-Mu lamulo lachiŵili, Mulungu akutilamula ife kuti tisadzipangire tokha fano lina lililonse losema ndi mitengo kapena miyala, kapena kudzipembedza zimenezi.

-Kodi chifukwa chiyani sitili oyenera kuti tidzipanga zinthu zomufananizira Mulungu?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi mzimu.
-Chifukwa chakuti Mulungu sawoneka ngati munthu, kapena nyama kapenanso mbalame.

-Ngati tikuzipembedza zinthu zimene anazilenga Mulungu, m’malo momupembedza Mulunguyo, ndiye kuti tikuchitsogoza chinthucho m’malo mwa Mulungu, chomcho ndiye kuti tikuphwanya lamuloli.

-Ngati sitikumupembedza Mulungu tsiku lina lililonse, ndikumaŵatsata maganizo athu kapena maganizo a anthu ena, ndiye kuti tikuphwanya lamuloli.

-Mulungu akulankhula kuti anthu onse aphwanya lamuloli.

-Chilango chophwanya lamuloli ndi imfa yosatha mu nyanja ya moto wosatha.

-Ili ndiye lamulo lachitatu limene Mulungu anapereka:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:7

7-“Musamaligwiritsire ntchito pa tchito zachabe dzina la Ambuye, Mulungu wanu, pakuti Ambuye



-Ngati tawona munthu wina ndikufuna kugona naye, ndiye kuti tikuliphwanya lamuloli.

-Mulungu akulankhula kuti anthu onse aphwanya lamuloli.

-Chilango chophwanya lamuloli ndi imfa yosatha mu nyanja ya moto wosatha.

-Ili ndiye lamulo lachisano ndi chitatu limene Mulungu anapereka:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:15

15-“Musabe.”

-Mu lamulo lachisano ndi chitatu, Mulungu akutilamula ife kuti tisabe zinthu za munthu wina.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu akuti tisabe zinthu za munthu wina?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anampatsa iyeyo mwayi wokhala ndi zinthuzo.

-Mulungu akuti ngati tikuganiza zakuba chinthu cha munthu wina, ndiyekuti tamubela kale munthuyo.

-Ngati tawona zinthu za munthu wina ndi kuganiza zokatenga zinthuzo kuti zikhale zathu, ndiye kuti taphwanya lamuloli.

-Mulungu akulankhula kuti anthu onse aphwanya lamuloli.

-Chilango chophwanya lamuloli ndi imfa yosatha mu nyanja ya moto wosatha.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu akuti tisamuphe munthu wina?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene amapereka moyo kwa anthu, ndiye Mulungu yekha ndi amene angawuchotsenso moyowo.

-Mulungu akulankhula kuti tikamuda munthu wina ndiye kuti tamupha munthuyo.
-Ngati tikuŵada anthu ena, ndiye kuti taphwanya lamuloli.

-Mulungu akulankhula kuti anthu onse aphwanya lamuloli.

-Chilango chophwanya lamuloli ndi imfa yosatha mu nyanja ya moto wosatha.

-Ili ndiye lamulo lachisano ndi aŵiri limene Mulungu anapereka:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:14

14-"Musachite chigololo."

-Mu lamulo lachisano ndi aŵiri, Mulungu akutilamula ife kuti tisachite chigololo ndi mkazi wina kapena wa mundthu wina koma wathu yekha.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu akutilamula kuti tisachite chigololo ndi mkazi wina kapena mkazi wa munthu wina?
-Chifukwa chakuti Mulungu anampereka mkazi kuti akhale wa mamuna m'modzi, ndiponso mamuna kuti akhale wa mkazi m'modzi.

-Mulungu akuti ngati tikumuyang'anitsitsa munthu wina, ndikumukhumbira titachita naye chigololo, ndiye kuti tachita naye kale chigolololocho.



sadzalephera kupereka chilango kwa munthu amene akuligwiritsira ntchito dzina Lake pa ntchito zachabe."

-Mu lamulo lachitatu, Mulungu akutilamula ife kuti tisamaliyalutse dzina la Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani ife tiyenera kulilemekeza dzila la Mlungu?
-Chifukwa chakuti dzina la Mulungu ndi Mulungu ndi chimodzimodzi.
-Chifukwa chakuti dzina la Mulungu ndi Mulungu ndi zimodzi.

-Ngati sitinalitchule dzila la Mulungu molemekeza, ndiye kuti ife sitinamulemekeze Mulungu, chomcho ndiye kuti tikuliphwanya lamuloli.

-Ngati tikulitchula dzina la Mulungu mosasamala, ndiye kuti sitikumutchula Mulungu, chomcho ndiye kuti taphwanya lamuloli.

-Ndi chinthu choyipa kwambiri kuti mwana asamaŵalemekeze anthu akuluakulu.

-Ndi chinthu choyipa kwambiri kuti munthu asamamulemekeze Mulungu.

-Mulungu akulankhula kuti anthu onse aphwanya lamuloli.

-Chilango chophwanya lamuloli ndi imfa yosatha mu nyanja ya moto wosatha.

-Ili ndiye lamulo lachinayi limene Mulungu anapereka:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:8-11

8-“Mudzilikumbukira tsiku la Sabata kuti likhale tsiku lopuma.

9-Masiku asano ndi limodzi, mudzigwira ntchito zanu zonse.

10-Koma pa tsiku la chisano ndi aŵiri, ndi tsiku lopuma chifukwa cha Ine, Ambuye, Mulungu wanu, pa tsiku limeneli inu musagwire ntchito, kapena ana anu, kapena a ntchito anu, ngakhalenso nyama zanu kapena alendo amene ali pakati panu.

11-Pakuti pa masiku asano ndi limodzi, Ambuye anamaliza kulenga kumwamba, dziko la pansi ndi nyanja. Ndi zinthu zonse za m’menemo, koma pa tsiku la chisano ndi aŵiri anapuma, ndi chifukwa chake Ambuye analidalitsa ndikuliyeretsa tsiku la Sabata.”

-Mu lamulo lachinayi, Mulungu akutilamula ife kuti tidzilisunga tsiku lachisanu ndi aŵiri ngati tsiku losankhidwa kuti tidzipuma.

-Kodi chifukwa chiyani tiyenera kupuma tsiku limodzi pa sabata?
-Chifukwa chakuti Mulungu analenga dziko la pansi ndi kumwamba pa masiku asano ndi limodzi, ndipo anapuma pa tsiku lachisano ndi aŵiri.

-Mulungu akutilamula ife kuti tidzipuma pa tsiku lachisano ndi aŵiri, kuti tidziziganizira zinthu zonse zimene Mulungu anatipangira ufe.

-Ngati sitiziganizira zinthu zimene Mulungu anatipangira, ndiye kuti tikuliphwanya lamuloli.

-Mulungu akulankhula kuti anthu onse aphwanya lamuloli.

-Chilango chophwanya lamuloli ndi imfa yosatha mu nyanja ya moto wosatha.



-Ili ndiye lamulo lachisanu limene Mulungu anapereka:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:12

12-”Mudziŵalemekeza bambo ndi mayi anu, kuti masiku a moyo wanu achuluke m’dziko limene Ambuye, Mulungu wanu, akukupatsani.”

-Mu lamulo lachisano, Mulungu akutilamula ife kuti tidziŵalemekeza bambo ndi mayi athu.

-Kodi chifukwa chiyani tiyenera kuti tidziŵalemekeza bambo ndi mayi athu?
-Chifukwa chakuti Mulungu anatipatsa ife bambo ndi mayi athu kuti adzitilera.

-Ngati sitikuŵamvera bambo athu, ndiye kuti tikuliphwanya lamuloli.
-Ngati sitikuŵamvera mayi athu, ndiye kuti tikuliphwanya lamuloli.

-Mulungu akulankhula kuti anthu onse aphwanya lamuloli.

-Chilango chophwanya lamuloli ndi imfa yosatha mu nyanja ya moto wosatha.

-Ili ndiye lamulo lachisano ndi chimodzi limene Mulungu anapereka:

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 20:13

13-“Musaphe.”

-Mu lamulo lachisano ndi chimodzi, Mulungu akutilamula ife kuti tisamuphe munthu wina.